

Muzilandira Uphungu Modzichepetsa

Davide ndi Bati-seba—Gawo 2

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Mukamawerenga mavesiwo, mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a mu nkhanayi akumvera mu mtima mwawo.

Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhanayi: Davide ndi Natani

Chidule cha nkhanayi: Ngakhale kuti Davide anakhululukidwa tchimo lalikulu limene anachita, anakumanabe ndi mavuto oopsa amene anabwera chifukwa cha tchimolo.

1

GANIZIRANI ZIMENE ZINACHITIKA.—WERENGANI 2 SAMUELI 12: 1-24.

Kodi mukuganiza kuti Natani ankaoneka bwanji pamene ankalankhula ndi Davide? _____

Kodi mukuganiza kuti mawu a Natani ankamveka bwanji pamene ankafotokoza fanizo la munthu wosauka ndi mwana wa nkhsosa? _____

Kodi mukuganiza kuti Natani anasintha bwanji kamvekedwe ka mawu ake pamene amafotokoza mosapita m'mbali tanthauzo la fanizoli muvesi 7 mpaka 9? _____

2

FUFUZANI MOZAMA.

N'chifukwa chiyani Natani ayenera kuti anaganizira mozama nkhanayi asanapite kukaonana ndi Davide? _____

Kodi inuyo mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Natani anagwiritsa ntchito fanizoli pofuna kuthandiza Davide? _____

Kodi Natani anatani pofuna kuthandiza Davide kuti aone kufunika kuchita zinthu mwachilungamo, ndipo n'chifukwa chiyani zimene Natani anachitazi zinali zothandiza kwambiri kusiyana ndi kukakamiza Davideyo kuti alape? _____

M'nkhanayi, zikuoneka ngati Yehova anakhululukira Davide mofulumira kwambiri. (*Werenganinso vesi 13.*) Koma kodi Yehova amaona chiyani chimene anthufe sitingachione mwa munthu mnzathu? _____

Kodi mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani mavuto amene Davide akanakumana nawo chifukwa cha tchimo limene anachita anali oyenerera? (*Werenganinso vesi 10-12, 14.*) _____

3

GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA.

Lembani zimene mwaphunzira zokhudza . . .
Kufunika kokhala munthu wodzichepetsa. _____

Mavuto amene munthu amakumana nawo akachita tchimo. _____

Chifundo cha Yehova. _____

4

DZIFUNSENI KUTI:

Kodi ndi zinthu ziti zimene zinachititsa kuti ndipatsidwe uphungu kapena ndidzudzulidwe? _____

Kodi ndingatani kuti ndisamanyinyirike ndikapatsidwa uphungu? _____

N'chifukwa chiyani tikunena kuti kupatsidwa uphungu kapena kudzudzulidwa, kumasonyeza kuti Yehova amatikonda? (ZOKUTHANDIZANI: Werengani Aheberi 12:5, 6.) _____

M'nkhaniji, kodi ndi mfundo iti imene yakukhudzani mtima kwambiri, ndipo n'chifukwa chiyani? _____

Mungachite izi: Lembani zimene mukuganiza kuti zikanachitika ngati Davide akanapanda kuvomereza zoti wachita tchimo, mwinsano kulanga Natani chifukwa chomupatsa uphunguwo. Kodi mukuganiza kuti zimenezi zikanakhudza bwanji mmene Yehova akanaweruzira mlandu wa Davide?

